Examination No:_________________________

# MKUKULA ZONE EXAMINATION BOARD

**2024 - 2025 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATION**

**STANDARD 8**

## CHICHEWA

**(100 MARKS)**

**Subject number: P032**

**Time allowed: 2hr 15 min**

**Date: ____/_____/ 2025**

**DZINA LANU:** ______________________________________________
***(Surname first)***

**DZINA LA SUKULU YANU:** ______________________________________

**Instructions**

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi atatu.**
2. Pepala ili lili ndi magawo anayi: **Gawo A, B, C** ndi **D.**
3. Lembani **dzina** lanu ndi **dzina la sukulu** yanu pamwamba pa tsamba lilionse.
4. Lembani chimangilizo mu **Gawo A** ndipo muyankhe mafunso onse mu **Gawo B, C ndi D.**
5. Perekani kwa okuyang'anilani kulemba mayeso (**imvijireta**) pepala lonseli nthawi ikakwana

| Question Number | Tick question if answered | Do not write in these columns | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6- 45 | | | |
| | | | |

Examination No:_________________________

## GAWO A (30 malikisi)

**Langizo: yankhani fuso limodzi lokha** mwa mafuso awiri omwe ali m'musiwa. Sankhani chimangilizo kapena kalata. Mau a chimangilizo chanu kapena kalata yanu **asachepele 100 ndipo asabzole 150.**

1. Lembani chimangilizo pa mutu uwu.
   "kusitha kwa nyengo" mwazina tsatilani izi polemba

   ***Ndime yoyamba***
   - Zitsanzo za kusintha kwa nyengo
   - Zomwe zikuchititsa kuti nyengo isinthe

   ***Ndime yachiwiri***
   - Mavuto omwe adza Kamba kakusintha kwa nyengo
   - M'mene mavuto akusintha kwa nyengo akhudzila miyoyo ya anthu
   - M'mene mavuto a kusintha kwa nyengo akhudzila dziko lapansi

   ***Ndime yachitatu***
   - Zomwe tingachite kuti tithane ndikusintha kwa nyengo

**Kapena**

2. Lembani kalata kwa amalume anu yopempha ndalama zoti mukalipire kusukulu ya sekondale yomwe mwasankhidwilako. Mwazina tsatilani izi polemba

   ***Ndime yoyamba***
   - Cholinga cha kalata yanu
   - Dzina la sekondale yomwe akusankhilaniko
   - Tsiku lotsekulila sukulu

   ***Ndime yachiwili***
   - Ndalama yomwe ikufunika ku sukuluko
   - Zinthu zomwe makolo anu akwanitsa kupeza
   - Kufunika kwa nthandizo lomwe mukupempha

   ***Ndime yachitatu***
   - Chisangalalo chanu pakupezeka kwa thandizo la ndalamazo.

Examination No:___________________________

Examination No:_________________________

**GAWO B** (20 malikisi)

Kumvetsela nkhani

3. Werengani nkhani yotsatilayi mosamala kwambiri kenako muyankhe mafuso otsatilawa

Chitamenyetsedwa chitsekocho, kudalowa njonda ya malamulo ovuta, simunamvekenso phokosi m'kalasimo ndipo ophunzira adangoti zyoli. Ankadziwiratu kuti m'phunzitsi wawo a Tumweretu samaonetsa chitsakano pa nkhani zoduka mutu.

"Mwalephera bwanji chonchi ntchito yanga?" adakwiya a Tumweretu.Umu nkuti akumasula lamba wa buluku lake, ndipo ena adaganiza kuti kunali kuyamba kwa ziwala m'maso kwa munthu wa nzeruyu.

"Amene walakwa zisanu alandira malamba asanu ndipo yemwe wakhoza zonse anyadire mizimu ya kwawo"." Ine kung'amba kukamwa konse kuja ndangozithira tsabola m'maso? "
Posachedwa mudamveka phokoso lakukwapulidwa m'kalasi muja.

Asanamalize kukwapula ophunzira ozizira bongo, padamveka kugogoda pachitseko. Atatuluka m'phuzitsiyo adati," Ukuchokera kuti nthawi ino? Makope ako ali kuti? Muli chiyani m'thumbamo?". Sikadayankhe kamwana kadachedwako,botolo la thobwa liri m'manja. Kenaka kadangotulutsa botolo lina. "Koma iwe zoona ungaiwale kutenga makope n'kukumvbukira thobwa ndi chimanga chokazinga?". Bwelerani baba mukapitirize kumwa thobwa n'kudyera chimanga chanucho." Kamwanako kanangotembenuka n'kuona msana wa njira.

Atabwelera m'kalasi a Tumweretu adagwidwa ndi mantha, msungwana yemwe adamalizira kumukwapula adali lamba pansi." Zione, Zione adaitana mphuzitsi uja." "Tadzuka". Zione sanayankhe. Maso ake adali chitsekere." Kalanga ine! Zione wakomoka eti?" anatero Tumweretu thukuta lili kamu kamu.

***Tsopano yankhani mafuso otsatilawa.***

a. Kodi a Tumweretu adali yani?
_____________________________________________ (1 malikisi)

b. N'chifukwa chiyani ophunzira adangoti zyoli m'kalasi muja?
_____________________________________________
_____________________________________________ (2 malikisi)

c. Fotokozani chifukwa chimene Tumweretu adakwapulira ophunzira?
_____________________________________________
_____________________________________________ (2 malikisi)

d. Kodi a Tumweretu amatathauzanji ponena kuti "amene walakwa zisanu alandila malamba asanu"?
_____________________________________________
_____________________________________________ (2 malikisi)

e. Ndani adagogoda pachitseko pomwe a Tumweretu amawalanga ophunzira aja mkalasi?
_____________________________________________ (1 malikisi)

f. Nanga kamwana kochedwa kaja kadali katatenga chiyani?
_____________________________________________ (1 malikisi)

g. Mukuganiza kuti a Tumweretu adali ndi khalidwe lotani?
_____________________________________________
_____________________________________________ (2 malikisi)

h. Perekani mvekero ndi mfuwu umodzi munkhaniyi.

________________________________________________________

___________________________________________________ (2 malikisi)

i. N'chifukwa chiyani a Tumweretu adagwidwa ndi mantha?

________________________________________________________

___________________________________________________ (2 malikisi)

j. Mukanakhala kholo la Zione mukadatani?

________________________________________________________

___________________________________________________ (2 malikisi)

k. Perekani matanthauzo a mawu awa:
Kuona msana wa njira ________________________________________

___________________________________________________ (2 malikisi)

l. Perekani mutu wankhaniyi.
___________________________________________________ (1 malikisi)

## GAWO C (10 malikisi)

*Yankhani mafuso onse awili m'gawoli*

4. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo
"Tsopano ndimulore kuti aloze yekha yemwe adampatsa chinjacho. Akatero timtengera pena."
***Mafunso***

a. (i) Tchulani mtundu wa malonje omwe mwawerengawo.
________________________________________________ (1 malikisi)

(ii) Kodi mawu oti "chinjacho" akutanthauzanji?
________________________________________________ (1 malikisi)

(iii) Kodi mukuganiza kuti angayankhule mawu amenewa ndani?
________________________________________________ (1 malikisi)

b. Kodi munthu oyenda pansi ayenera kuyenda mbali iti ya nsewu?
________________________________________________ (1 malikisi)

c. Tchulani mchitidwe umodzi omwe umalepheretsa atsikana kumaliza maphunziro awo.
________________________________________________ (1 malikisi)

5. Kupanga ziganizo
*Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:*

a. Njakata

____________________________________________________

________________________________________________ (1 malikisi)

b. Mkoko

____________________________________________________

________________________________________________ (1 malikisi)

c. Ndi

____________________________________________________

________________________________________________ (1 malikisi)

d. Tafulira

____________________________________________________

________________________________________ (1 malikisi)

e. Zalende

______________________________________________________________

__________________________________________ (1 malikisi)

**GAWO D** (40 malikisi)

***Mafuso 6 mpaka 10****: Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatilazi.*

6. Naliyela wavala <u>bwino.</u>
   a. Mfotokozi
   b. Mneni
   c. Muonjezi
   d. Mperekezi
7. <u>Lamulo</u> loposa onse ndikukonda mzako.
   a. Dzina
   b. Muonjezi
   c. Mfotokozi
   d. Mneni
8. Mayi Mbewe amaganiza <u>mofatsa.</u>
   a. Mperekezi
   b. Mfuwu
   c. Mneni
   d. Muonjezi
9. Katangale <u>ndi</u> oyipa.
   a. Mfotokozi
   b. Mneni
   c. Mlumikizi
   d. Dzina
10. <u>Imodzi</u> yapezeka mnyumba ya a Bwande
    a. Dzina
    b. Mperekezi
    c. Mfotokozi
    d. Mlowam'malo

***Mafuso 11 mpaka 15****. Sankhani mitundu ya alowam'malo omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'zianizo zotsatilazi.*

11. Tawona <u>iwo</u> akusodza somba.
    a. Woloza
    b. Wamgwirizano
    c. Wa umwini
    d. Wa dzina lake lake
12. <u>Ine</u> ndipita mawa.
    a. Wotsimikiza
    b. Woloza
    c. Wofunsa
    d. Wa umwini
13. <u>Zimene</u> wandipatsa ndi izi.
    a. Wa mgwirizano
    b. Wowerenga
    c. Wotsindika
    d. Woloza
14. Agwira <u>zochepa</u> lero.
    a. Wofunsa
    b. Wa dzina lake lake
    c. Wochuluka
    d. Wowerenga
15. <u>Awo</u> akhoza mayeso.
    a. Woloza
    b. Wa umwini
    c. Wamgwirizano
    d. Wofunsa

***Mafunso 16 mpaka 20.*** *Sankhani mawu otsutsana m'matanthauzo ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo.*

16. Ife tadya <u>mfwisuro</u>.
    a. Kadzutsa
    b. Mgonero
    c. Madyerero
    d. Nkhomaliro
17. Alimi amachita ulimi wa mthilira nyengo ya <u>mwamvu</u>.
    a. Ng'amba
    b. Dzinja
    c. Mkucha
    d. Chilimwe
18. Mbava zikagwidwa zimaona <u>zodamutu</u>.
    a. Tsoka
    b. Mwayi
    c. Nzeru
    d. Mavuto
19. Mwana <u>watsitsimuka</u> atangodya phala.
    a. Wakomoka
    b. Wadzimbidwa
    c. Wakhuta
    d. Wasangalala
20. Ku <u>gomo</u> kuli njoka.
    a. Dera
    b. Manda

c. Phiri
d. Chigwa

***Mafunso 21 mpaka 25.*** *Samkhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro zoyenera za m'kalembedwe mziganizo zotsatirazi.*

21.
a. Mwana wathawitsa mbalame.
b. mwana wathawitsa mbalame.
c. Mwana, wathawitsa mbalame.
d. Mwana wathawitsa mbalame

22.
a. abambo adati," Choka iwe mwana wakuba."
b. Abambo adati," Choka iwe mwana wakuba".
c. Abambo adati," choka iwe mwana wakuba!"
d. Abambo, adati choka iwe mwana wakuba!

23.
a. Aaa, mwabwera nokhanokha?
b. Aaa! Mwabwera nokhanokha?
c. Aaa? Mwabwera nokhanokha.
d. Aaa, mwabwera nokhanokha

24.
a. Kodi mwadya!
b. Kod, mwadya
c. Kodi? mwadya.
d. Kodi mwadya?

25.
a. Ndithudi. ife tapambana mayeso.
b. Ndithudi ife, tapambana mayeso.
c. Ndithudi ife tapambana, mayeso.
d. Ndithudi, ife tapambana mayeso.

***Mafunso 26 mpaka 30.*** *Sankhani mawu oyenera kutsiriza zifanifani zotsatirazi.*

26. Kuchita msangala ngati ___________?
a. Pumbwa
b. Mkango
c. Mphaka
d. Namtchengwa

27. Kuwala ngati _______________?
a. Nyali
b. Dzuwa
c. Nyenyezi
d. Mwezi

28. Kusakhuta ngati _____________?
a. Chule
b. Kumanda
c. Nkhuku
d. Mbuzi

29. Kuipa ntima ngati _______________?
a. Wakuba
b. Mfiti yayikazi
c. Munthu osasamba
d. Wothena agalu

30. Ukhondo ngati ______________?
a. Nkhosa
b. Mavu
c. Mphaka
d. Ngumbi

***Mafunso 31 mpaka 35.*** *Sankhani matanthauzo a ndagi zotsatirazi.*

31. Ndidzayera nkadzafa.
a. Nkhuku
b. Nkhumba
c. Gwape
d. Mbuzi

32. Chimbalame chalavula anthu a moyo.
a. Ndege
b. Galimoto
c. Nyumba
d. Kakowa

33. Agogo anga Malaya awo ndi minga.
a. Chipwete
b. Mtengo waminga
c. Nungu
d. Kankhande

34. Kwake nkutola akudya ndi ena.
a. Kamwa
b. Dzanja
c. Mano
d. Milomo

35. Si mfumu koma mwini sitolo.
a. Nyakwawa
b. Nduna
c. Mfumu yayikulu
d. Mmwenye

***mafunso 36 mpaka 40.*** *Sankhani matanthauzo azining'a zotsatirazi.*

36. Wopanda manyazi.
a. Wothothoka sidze
b. Njinga
c. Wamtali manja
d. Walinyonyo

37. Alangizi akhalira nkhani.
    a. Azengereza
    b. Apondereza
    c. Akondera
    d. Asokoneza

38. Ndipsi zimasokoneza m'dziko.
    a. Munthu wamwano
    b. Munthu wa ulesi
    c. Munthu wauve
    d. Munthu wakuba

39. Kuyenda utsi uli tsitu.
    a. Kupusa
    b. Kuyenda mofatsa
    c. Kusinza
    d. Kuyenda utatsizina

40. Mnyamata uja adadya matako agalu.
    a. Munthu wonama
    b. Munthu wokonda kudya nyama
    c. Munthu omwa mowa
    *d.* Munthu oyendayenda

***Mafunso 40 mpaka 45**. Sankhani mitundu ya nthambi ya ziganizo zosaima pazokha zom we zili ndi mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.*

41. Adaulula zomwe adagwirizana.
    a. Ya muonjezi
    b. Ya dzina
    c. Ya mfotokozi
    d. Yosaima payokha

42. Ng'ombe yomwe waphayi ndi yanga.
    a. Ya dzina
    b. Ya muonjezi
    c. Ya mfotokozi
    d. Ya muonjezi

43. Mnyamata akuyenda ngati wadwala.
    a. Yoyima payokha
    b. Ya dzina
    c. Ya mfotokozi
    d. Yosayima payokha

44. Zoti adapita kusukulu, ndi zoona.
    a. Ya dzina
    b. Yoyima payokha
    c. Ya muonjezi
    d. Ya mfotokozi

45. Muuzeni avine monga akufunira.
    a. Ya dzina
    b. Ya muonjezi
    c. Yoyima payokha
    d. Ya mfotokozi

**MAFUNSO ATHERA APA**